# Ayendera pulojekiti yaikulu ya mthirira

WOLEMBA:
ESMIE KOMWA

Wachiwiri kwa nduna ya zaulimi m'dziko muno Agness Nkusankhoma adayendera ntchito zomangamanga zaulimi wothirira umene ukudziwika kuti Shire Valley Transformation Project (Svtp) lachinayi m'boma la Chikwawa.

Ndunayi idati cholinga chake chidali chofuna kuona ntchito zomangamanga za mthirirawu pamene zafika.

Iye adafotokoza kuti ntchitoyi ikuyenda bwino chifukwa adapeza zinthu zina zachilendo zimene zamangidwa pamalowa kuonjezera pa zimene adaziona nthawi ya m'mbuyomo pamene adakayendera.

"Monga tikudziwira kuti mthirira woterewu ndiwaukulu kwambiri komanso ndiwoyamba kumangidwa m'dziko muno tili ndi chikhulupiriro kuti akamaliza kumanga udzatukula anthu okhala m'chigwa cha mtsinje wa Shire ndi dziko lonse lino.

"Kontalakitala wanditsimikizira kuti akumanga molimba kwambiri choncho dziko lino lidzakhala likugwiritsa ntchito mpaka kalekale," adatero Nkusankhoma.

Nkusankhoma adati mthirirawu uthandiza alimi m'chigwachi kulima mbewu zochuluka kusiyana ndi kale pamene amakanika ngakhale kukhala ndi chakudya chokwambira kaamba ka ng'amba ndi kusefukira kwa madzi kumene kumaphsyinja kwambiri ulimi m'chigwachi.

Malingana ndi mkulu woonelera ntchito zochitika ku pulojekitiyi



CHITHUNZI: ESMIE KOMWA

**Nkusankhoma (pakati) kumvetsera mmene ntchitoyi ikuyendera**

Chitsanzo Kamowatimwa, ntchito za mu gawo loyamba zimene zoyambirira ndi kumanga ngalande yokwana makilomita 6 ndi potengera madzi yafika pa 50.2 pelesenti.

Iye adati gawo loyamba la ntchitoyi ndi kumanga potengera madzi ndi ngalande yokwana makilomita 52 kuchokera pa damu la Kapichira kulekezera pa Lengwe.

"Makilomita 46 a ngalande otsalawo akuyembekezeka kuyambidwa mu mwezi wa October chaka chomwe chino ndipo gawo lonse loyamba likuyembekezeka kutha mu mwezi wa December chaka cha 2023.

"Bwenzi pano tili pa 60 pelesenti koma matenda a covid ndi amene achedwetsa chifukwa tatsekerako kokwana kawiri konse kaamba ka vutoli komanso zipangizo ndi anthu ena amene amayenera kubwera kudzagwira ntchitoyi sadafike mu nthawi yake," adafotokoza motero.

Mthirirawu ukuyenera kumadzathirira madzi pa minda yokwana mahekitala osachepera 43 000 ukamalizika ndipo gawo loyamba likumangidwa ndi ndalama zochokera ku World Bank, Africa Development Bank, The Global Environment Facility, Opec Fund for International Development (Ofid) ndi boma la Malawi. ■

## KODI MUKUDZIWA?



Kuti mukhoza kulima mbewu osagwiritsa ntchito feteleza ndi mankhwala?

Nanga mukudziwa kuti kulima m'mizere kumapha malo ochuluka obzalamo mbewu komanso kumaika njira zambiri za madzi?

Kwa alimi amene akuchita ulimi wosaguga umene umadziwika kuti permaculture pa chizungu akutsimba lokoma.

**KALIMALIMA** James Kazembe

